# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NTCHISI M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.

Boma la Dedza likuyembekezeka kulandira **mvula yopitítilila mlingo wokhazikika**.


## October 2024




M'mwezi wa October, madera ambiri adzalandira mvula yochepera 50mm. Mlingo wu ndi wokhazikika m'mwezi wa October m'bomali.

Mphepo yamkutho chifukwa chakutetha ikuyembekezeka mwezi wa October.


## November 2024




M'mwezi wa November, tikuyembekezera madera ena kulandila mvula ya mlingo ofika 100mm. Komabe, mvula yambiri ikuyembekezeka kuyamba sabata lachiwili la December

Tiyembekezerenso mphepo yamkutho komanso mphezi.


## December 2024




Madera ambiri adzalandila mvula ya mlingo wokhazikika ngakhale madera ena adzalandila mvula ya mlingo wochepera mlingo okhazikika. Mvula ikuyembekezeka kuyamba pakati pa sabata lachiwiri ndi sabata la chitatu la mwezi wu.


Madera ambiri akuyembekezeka kulandila mbvula la pafupifupi 200mm.

## January 2025





M'mwezi wa January, ulosi ukusonyeza mvula yopitilila mlingo wokhazikika.
Madera ambiri akumwera kwa TA Tambala ndi TA Kaphuka, akuyembekezeka kulandila mbvula yopitilila 300mm, pomwe madera ena akumadzulo kwa TA Pemba ndi SC Chauma akuyembekezeka kulandila mvula ya pakati pa 200mm 250mm.

## February 2025




mvula ikuyembekezeka kugwa ya mlingo okhazikika. Komabe madera ena akumwera kwa TA Kaphuka komanso ku mphoto kwa TA Kachindamoto akuyembekezeka kulandila mbvula yochepera mlingo wokhazikika. Madera ena a kwa TA Tambala akuyembekezeka kulandila mbvula ya mlingo wapafupifupi 250mm. Tiyembekezere ng'amba yopitilila sabata limodzi m'weziwu


## March 2025




Mvula ya mlingo opitilila mlingo okhazikika ikuyembekezeka kugwa.
Madera ambiri a kwa TA Kachindamoto akuyembekezeka kulandila mbvula yochepera mlingo okhazikika ndipo madera wa akuyembekezeka kulandila mbvula ya pafupifupi 150mm.
Madera akumwera kwa TA Tambala akuyembekezeka kulandila mbvula ya pafupifupi 250mm.

*Boma la Dedza likuyembekezeka kulandira mvula* ***yopitilila mlingo wokhazikika m'dzinja la 2024-2025****. Mvula ikuyembekezeka kuyamba pakati pa sabata lachiwiri la December ndi sabata lachitatu la December 2024 ndikutha pakati pa sabata la chitatu la mwezi wa march ndi sabata la chiwiri la April 2025. Nyengoyi ikuyembekezeka kukhala ya pakati pa masiku 110 mpaka 120.*
*Pali kuthekera kwakukulu kokhala ndi ng'amba yopitilila sabata imodzi m'mwezi wa February. Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ku Dedza yaperekedwa pansipa;*


## April 2025




Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kutha pakati pa sabata la chinayi la mwezi wa March ndi sabata la chiwiri la mwezi wa April.

Komabe, pali kuthekera kuti madera ena akuyembekezeka kudzalandila mvula pafupifupi 50mm kapena kupitilila.

| DEDZA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 1.1 | 12.1 | 10.1 |
| NOV | 29.6 | 76.7 | 27.0 |
| DEC | 143.5 | 221.3 | 187.3 |
| JAN | 205.4 | 277.8 | 310.1 |
| FEB | 174.5 | 259.8 | 177.5 |
| MAR | 108.2 | 171.4 | 202.9 |
| APR | 18.6 | 54.5 | 45.6 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com